# CHIKOWI ZONE

## 2023 Primary School Leaving Certificate Mock Examination

## CHICHEWA

(100 MARKS)

DATE:

Subject Number: P199

Time allowed: 2 hours 15mins

11:30 – 1:45 pm

Name of Candidate: ______________________________

(Surname First)

Name of School: ______________________________

Malangizo

1. Pepalali lili ndi masamba asanu ndi atatu **(8)** chonde onani.
2. Lembani dzina lanu ndi dzina la sukulu yanu mumpata mwapatsidwa pamwambapa.
3. Pepalali lili ndi magawo anayi A, B, C ndi D ndipo muyankhe mafunso onse.
4. Lembani yankho la mu gawo A pa pepala lomwe mwapatsidwa
5. Yankhani mafunso a mu Gawo B ndi C mmipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lililonse
6. Yankhani mafunso a mu Gawo D pozungulizo lembo lokhala ndi yankho lanu lolondola
7. Kumbukirani kupereka pepalali kwa oyang'anira mayeso nthawi ikakwana yoti musiye kulemba

| Question number | Tick if answered | Do not write in these columns | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 – 45 | | | |
| | | | |

©all rights reserved

Turn over

## Gawo A: 30 Malikisi

LANGIZO

- *Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'musiwa.*
- *Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata*
- *Mawu achimangirizo kapena kalata asachepele  100 koma asabze 150*

1. Lembani chimangirizo pamutu uwu: "**ULENDO OSAIWALIKA M'MOYO WANGA**"
   Mwazina tsatani izi polemba
   **Ndime yoyamba:**
   - Komwe munapita pa ulendowo
   - Tsiku lomwe munayenda ulendowo
   - Chomwe munakachita ku ulendowo

   **Ndime yachiwiri:**
   - Mayendedwe anu popita ndi pochokera ku ulendowo
   - Zabwino zomwe munakaona komwe munapitako
   - Zovuta zomwe munakumana nazo pa ulendowu

   **Ndime yachitatu:**
   - Chomwe mungalangize mnzanu za ulendo

**KAPENA**

2. Lembani kalata kwa mnzanu yomufotokozera za phwando lomwe mwakonza

   **Ndime yoyamba:**
   - Phwando mwakonza chifukwa ninji?
   - Tchulani malo,tsiku ndi nthawi yomwe phwando lidzachitikere

   **Ndime yachiwiri:**
   - Tchulani magule kapena zosangalatsa zina zomwe zidzakakhalepo pa phwandolo
   - Fotokozani N
   - njira zina zomwe mwagwiritsa ntchito kutumizira mauthenga
   - Mukuganiza kuti kudzakhala anthu angati?

   **Ndime yachitatu:**
   - Kodi phwando lanulo lidzakhala lopambana bwanji?
   - Kodi phwandolo lidzakupindulira chiyani?



©chikowi zone - 2023

GAWO B: (20 MALIKISI)

3. **Werengani nkhaniyi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo.**



©chikowi zone - 2023

Mudzi utatha kumanda, mdzukulu m'modzi adapita kukauza amfumu Gobede kuti mwambo wa maliro uyambe. Amfumu atakaona kutha kwa mudziwo, mosakhalitsa adzukulu adatulukira atandonda ngati midzodzo chithatha chili m'manja. Apa n'kuti wotsogolera mwambo atauzanso anamilira ndi anthu onse zoyamba mwambowo. Atatero anthu angapo adatulutsa mfumu napita kumsamba mfumu.

Wotsogolera mwambo adaimilira nayamba kuyankhula motere, "pepani anamalira nonse, pepani gogo chalo Mlindira, pepani amfumu Gobede ndi mafumu onse, pepani amayi ndi abambo, anyamata ndi asungwana nonse:"

Tsopano tikufuna tiyambe mwambo wa maliro. Chonde tiyeni tikhale chete kuti tipereke ulemu woyenera pa maliro komanso timvane. Tidziwa maliro alibe chizolowezi. Nanga tingatani poti ndi m'mene kunalembedwera motere; pepani, pepani anamalira nonse tiugwire mtima wathu. Posunga nthawi tipemphe oyankhula onse kuti ayankhule mwachidule. Poyamba tipemphe akuchikazi, akuchimuna kenako a mudzi uno kuti atiyankhule.

Ulemu kwa gogo chalo Mlindira! Ulemu kwa inu nonse mwadza kudzatikuta. Ine ndaima pano kuti ndiyankhule m'malo mwa anamalira onse akuchikazi ndi akuchimuna. Poyamba ndithokoze inu nonse pozatikuta anamalira ife pa nthawi yoliritsa ndi yosaiwalikayi. Tidziwa mwasiya ntchito zanu zonse podziwa kuti maliro nkulirana ife sitikadatha kuchita zonse tokha. Kachiwiri ndifotokoze matenda awatenga malemu agona apawa.

Malemuwa adagwa pomwe amati alowe mnyumba mwawo dzana mosazengereza tidapita nawo kuchipatala ku Chitalo komwe atawapima anawapeza ndi malungo aakulu. Mankhwala adalandira koma m'bandakucha wadzulo tidangoona akutilawira, mosakhalitsa kupita kudali komweko. Dandaulo lathu ndi la ana, adzukulu ndi mferekazi omwe malemuwa asiya. Zateremu mtengo wakachere wagwa.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa.**

a. Ndi ndani adapita kukauza mfumu kuti mudzi watha kumanda?
   ____________________________________________(2 malikisi)
b. Tchulani dzina la mudzi womwe mudachitikira maliro.
   ____________________________________________(2 malikisi)
c. N'chiyani chidachitika mwambo wamaliro usadayambe
   ____________________________________________(2 malikisi)
d. Kodi wotsogolera mwambo adayamba ndi chiyani m'malonje ake?
   ____________________________________________(2 malikisi)
e. Kodi anthu adapemphedwa chiyani kuti aonetse ulemu wawo pa mwambo wamaliro uja?
   ____________________________________________(2 malikisi)
f. Kodi anthu oyankhula pa mwambo wamaliro akadachitanji kuti asunge nthawi?
   ____________________________________________(2 malikisi)
g. Pezani m'nkhaniyi mawu omwe akufanana ndi awa:
   i. Dzenje lamanda
      ________________________________________(1 malikisi)
   ii. Bokosi



©chikowi zone - 2023

_____________________________________________(1 malikisi)

iii. Namfedwa

_____________________________________________(1 malikisi)

iv. Kukhazika

_____________________________________________(1 malikisi)

h. Kodi omwalirayo amadwala chiyani?

_____________________________________________(2 malikisi)

i. Perekani tanthauzo la mkuluwiko uwu “mtengo wakachere wagwa”

_____________________________________________(2 malikisi)

## GAWO C (malikisi10)

4. **Werengani kakhanika ndipo muyakhe manfunso otsatirawo.**
   Nkhani yomwe ndabwerera pano ndi yokuti akudandaula ndi makhalidwe oipa a ana athu,anawa sakumasamala katundu wasukulu ndipo adaphwanyanso magalasi m’mazenera.

**Mafunso**

a. Kodi ndi malonje anji mwawerengawa?

_____________________________________________

b. Kodi malonjewa akuchitikira kuti?

_____________________________________________

c. Kodi yemwe akuyankhula m’nkhaniyi ndi ndani?

_____________________________________________

d. Kodi malonjewa akupita kwayani?

_____________________________________________

e. Kodi wakwera njinga ayende mbali iti ya mseu?

_____________________________________________

5. **KUPANGA ZIGANIZO**
   **Pangani ziganizo zonveka bwino ndi mawu awa:**

a. Nkhuti

_____________________________________________

b. gwa

_____________________________________________

c. funtha

_____________________________________________

d. wanu

_____________________________________________

e. ndi

_____________________________________________

## GAWO D (MALIKISI 40)

*Zungulizani lembo lokhoza **(A, B, C ndi D)** mmafunsootsatirawa.*



©chikowi zone - 2023

**mziganizo zotsatirazi.**

6. Mwana wosamva amachititsa manyazi makolo.
   A mfotokozi B muonjezi
   C mneni D mlumikizi

7. Mchokocho wavuta zedi kubungwe lathu
   A mneni B dzina
   C mlowam'malo D muonjezi

8. Iye apita kwa achimwene ake mawa.
   A mvekero B mperekezi
   C muonjezi D mlumikizi

9. Dambuleni simphuzitsi.
   A mneni B mlumikizi
   C mperekezi D mlowam'malo

10. Mtengo udagwa kuti khu.
    A mneni B mfotokozi
    C mvekero D mlumikizi

**Mafunso 11 mpaka 15: Sankhani magulu amayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

11. Iye ali ndi mbuzi zitatu.
    A chi-,zi B i-,zi
    C li-,ma D u-,ma

12. Amayi agula chikwama chkongola.
    A mu-,a B i-,zi
    C chi-,zi D ka-,ti

13. Galimoto lagunda chule.
    A mu-,a B mu-,mi
    C i-,zi D chi-,zi

14. Atate agula khasu latsopano.
    A u-,ma B ka-,ti
    C li-,ma D chi-,zi

15. Richard sanabwere chifukwa akudwala.
    A i-,zi B chi-,zi
    C u-,ma D ku-,pa-,mu

**Mafunso 16 mpaka 20: Sankhani ntchito za maina atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

16. Fisi wagwira mbuzi.
    A loitanila
    B mtsiriza mneni
    C mwininkhani
    D pamnthera nkhani

17. Chimwemwe wabwera kuno
    A pathera nkhani
    B loitanira
    C mwini nkhani
    D mtsiriza mneni

18. A Banda apha galu.
    A loitanira
    B pamthera nkhani
    C mwini nkhani
    D lapadera

19. Yohane akusewera mpira.
    A mwini nkhani
    B mtsirizo wamneni
    C pamthera nkhani
    D wa malo

20. Nabanda, mdzakazi wapeza ntchito m'boma.
    A mwini nkhani
    B pamthera nkhani
    C dzina lapadera
    D loitanira

**Mafunso 21 mpaka 25: Sankhani mawu ofanana matanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

21. Agogo apita ku dondo.
    A mudzi B nkhalango
    C chimanga D mawere

22. Patha zaka zingapo ali kumasano.
    A kumunda B kunja kwa dziko
    C kumanda D kunyanja

23. Anthu ambiri abzala mbwani chaka chino.
    A mbatata B chinangwa
    C nzama D chimanga

24. Mwana wa mwano salandila mphoto.
    A ntudzu B nkano
    C nkhanza D ukali

25. Kalowa m'malaya sachoka nyumba muno.



©chikowi zone - 2023

A njala B nsanje
C usiwa D wakuba

**Mafunso 26 mpaka 30: Sankhani mtundu wa msintho wa mneni omwe ali ndi mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

26. Kapu yanga <u>idasweka</u>.
    - A womchitira
    - B wochitiridwa
    - C wochititsa
    - D wochitidwa mchibisira
27. Namwali wamwana uja <u>wamenywa</u>.
    - A wochititsitsa
    - B wonyazitsa
    - C wochitidwa poyera
    - D wochititsa
28. Emma <u>wabetsa</u> ndalama.
    - A wochitidwa B wochititsitsa
    - C wochititsaD womchitira
29. Aphunzitsi <u>amugulira</u> cholembera.
    - A wochitidwa
    - B wochitidwa m'chibisira
    - C wochititsa
    - D womchititsa
30. Njinga zija <u>zaombana</u>.
    - A wochitirana
    - B wochititsitsa
    - C wochititsa
    - D wobwerezabwereza

**Mafunso 31 mpaka 35: Sankhani chachimuna cha mawu atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

31. Ambewe adakwatira <u>chumba</u>.
    - A mfulu B nkamwini
    - C ntheno D gojo
32. <u>Nankungwi</u> adapereka mwambo kwa atsikana.
    - A wakunjira B mlangizi
    - C mtsogoleri D mphungu
33. <u>Ntchembere</u> zamasiku ano zilibe ulemu.
    - A anyamata B abambo
    - C ndoda D atambala
34. <u>Thadzi</u> wanga wasowa.
    - A tambala B chipsolopsolo
    - C mkota D mtheno
35. <u>Mkota</u> uwu ndi wonenepa
    - A nzinzi B mthoni
    - C mtheno D tonde

**Mafunso 36 mpaka 40: Sankhani mitundu ya aonjezi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

36. Anamlanga mwanayo <u>mwankhaza</u>.
    - A okana B ovomera
    - C wamchitidwe D wamuyeso
37. Bwerani <u>kuno</u> mudye nsima.
    - A wa malo B wa nthawi
    - C wa mchitidwe D wamuyeso
38. Abambo amapita kwawo <u>pafupipafupi</u>.
    - A wamawerengo B wamuyeso
    - C wokana D wamchitidwe
39. Mubwere kwathu <u>masana</u>.
    - A wanthawi
    - B wamalo
    - C wamuyeso
    - D wamchitidwe
40. Mwafika <u>bwanji</u> kuno?
    - A wa malo
    - B wowerenga
    - C wanthawi
    - D wofunsa

**Mafunso 41 mpaka 45: Sankhani mtundu wa nthambi zachiganizo zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwake mziganizo zotsatirazi.**

41. Ana <u>akubwera apowo</u> sindiwadziwa.
    - A yamuonjezi
    - B ya dzina
    - C ya mfotokozi
    - D yoima payokha
42. <u>Wezi akuwerenga buku</u> lomwe adagula dzana
    - A ya dzina
    - B yoima payokha



©chikowi zone - 2023

C ya mfotokozi
D ya muonjezi

43. <u>Zokuti ndi waulemu</u> ndi zoona.
A yamfotokozi
B yamuonjezi
C yoima payokha
D yadzina

44. Tidagwira ntchito <u>monga momwe adatiuzira</u>.
A yadzina
B yamfotokozi
C yamuonjezi
D yoima payokha

45. Galu <u>yemwe wachita misalayo</u> ndi wanga
A ya mfotokozi
B yadzina
C yoima payokha
D yamuonjezi

# MAFUNSO ATHERA APA



©chikowi zone - 2023